-Mtsogolomo, Yesu adzamuponya Satana ndi ziwanda zache zonse mu Nyanja ya Moto Wosatha.

-Pamene Yesu anatha kumugonjetsa Satana, Satana anamusiya Iye kwa nthaŵi ndithu.

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 4:11

11-Pomwepo Satana uja anamusiya Yesu, ndipo angero anafika kudzamutumikira Iye.

-Satana anamusiya Yesu kwa nthaŵi ndithu, ndipo Mulungu Atate anatumiza angero kudzamuthandiza Iye.

-Ngakhale kuti Satana anamusiya Yesu kwa nthaŵi ndithu, Satana anabweleranso kukamuyesa Yesu.



## PHUNZIRO LA 49

1. Kodi Yohane M'batizi ankaŵachita Ayuda kukhala okozekera ndani m'mitima mwawo?
-Yesu Mpulumutsi.

2. Kodi Yohane M'batizi ankayikomzekeretsa bwanji mitima ya Ayuda?
-Poŵaphunzitsa iwo Mawu a Mulungu.

3. Kodi Yohane M'batizi ankaŵaphunzitsa chiyani anthu?
-Yohane M'batizi ankaŵaphunzitsa Ayuda kuti atembenuke mitima yawo ku machimo.

4. Kodi kutembenuka mtima ku machimo kumatanthawuza kuti chiyani?
-Kutembenuka mtima kumatanthawuza kusintha maganizo athu pa Mulungu , ife ndi tchimo.
-Kutembenuka mtima kumatanthawuza kusintha maganizo athu pa Mulungu.

5. Kodi ubatizo umatanthawuza chiyani?
-Ubatizo ndi chidziŵitso chakuti inu mwavomereza machimo anu pa maso pa Mulungu, ndipo mukumupempha Mulungu kuti akupulumutseni.

6. Kodi ubatizo unatha kuŵapulumutsa Ayuda ku mphamvu ya sambi, imfa ndi Satana?
-Iyayi.

7. Kodi ndani yekha amene anakatha kuŵapulumutsa Ayuda ku mphamvu ya sambi, imfa ndi Satana?

-Yesu Mpulumutsi.

8. Kodi chifukwa chiyani Yohane M'batizi anaŵatcha Afarisi ndi Asaduki kuti ndi ana a njoka?
-Chifukwa chakuti Afarisi ndi Asaduki anali odzikweza kwambiri.
-Chifukwa chakuti Afarisi ndi Asaduki sanavomereze kuti iwo anali ochimwa kwa Mulungu.

9. Kodi chifukwa chiyani Afarisi ndi Asaduki ankaganiza kuti Mulungu ankasangalala ndi iwowo?
-Chifukwa chakuti iwo ankaganiza kuti ntchito zawo zingathe kumupangitsa Mulungu kusangalala.

10. Kodi ndi ntchito yanji imene yingamusangalatse Mulungu?
-Ntchito imene ingamusangalatse Mulungu kwa munthu aliyense ndi yotembenuka ku machimo yokha.

11. Kodi chifukwanso chiyani chimene ankaganiza Afarisi ndi Asaduki kuti Mulungu ankasangalala ndi iwo?
-Afarisi ndi Asaduki ankaganizanso kuti Mulungu anali osangalala ndi iwo chifukwa chakuti iwo anali zidzukulu za Abulahamu.

12. Kodi kukhala chidzukulu cha munthu wina wache, kungamupangitse Mulungu kusangalala ndi ife?
-Iyayi.

13. Kodi Yohane M'batizi analankhula chiyani za anthu onse amene ali odzikweza ndipo okana kuvomereza kuti iwo anamulakwira Mulungu?



-Ndi mawu a Mulungu.

-Kodi Yesu anaŵasemphanitsa mawu a Mulungu?
-Iyayi.

-Yesu analankhula mawu a Mulungu ngati m'mene analembedwera M'buku la Mulungu, Bayibulo.

-Pachiyambi, Satana anayesa kuti akhale ambuye wa Mulungu koma analephera.

-Kenako Satana anamunamiza Adamu ndi Eva kuti ife tisiyanitsidwe kwa Mulungu.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Eva anamumvera Satana, Satana anasanduka kukhala mbuye wa Adamu ndi Eva pamodzi ndi anthu onse.

-Tsopano Satana anayesa kuti akhale mbuye wa Yesu koma analephera.

-Kodi Yesu ndi Satana wamkulu ndani?
-Yesu.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu ndi wamkulu kuposa Satana?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu.

-Pachiyambi, Yesu ndi amene anamulenga Lusifala.

-Yesu anamulenga Lusifala ngati mngero opanda zomuyipitsa, koma Lusifala anachimwa ndipo anasanduka kukhala Satana.

ngati amugwadire ndikumupembedza iye.

-Kodi kunali kotheka kwa Satana kuti amupatse Yesu zonse za pa dziko la pansi?
-Inde.

-Kodi chifukwa chiyani kunali kotheka kuti Satana amupatse Yesu zonse za pa dziko la pansi?
-Chifukwa chakuti Adamu atamumvera Satana, iye anasanduka kukhala mbuye wa Adamuyo pamodzi ndi anthu onse a pa dziko la pansi.

-Pa nthaŵi imene Adamu anamumvera Satana, Satana anasanduka kukhala mbuye wa pa dziko lonse la pansi.

-Kodi Yesu anamupembedza Satana?
-Iyayi.

-Kodi Yesu anamuyankha chiyani Satana?

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 4:10

10-Yesu anati, “Choka iwe, Satana! Malemba akuti, “Udzikaŵapembedza Ambuye, Mulungu wako, ndipo udziŵatumikira iwo okha.”

-Yesu anabwerezanso kwa Satana zimene zinalembedwa M’buku la Mulungu, Bayibulo.

-Yesu anati kuti ife tidzimupembedza Mulungu yekha.

-Kodi Yesu anamupambana bwanji Satana?



-Analankhula kuti Mulungu adzaŵadula iwo ngati mtengo osabereka ndi kuŵaponya mnyanja ya moto osatha.

14. Kodi ndani amene ankamutsogolela Yesu pamene anali pa dziko la pansi pano?
- Mulungu Mzimu Oyera.

15. Kodi Mulungu Atate analankhula chiyani za Yesu?
-Mulungu Atate analankhula kuti Iye ali osangalala kwambiri ndi Yesu.

16. Kodi chifukwa chiyani Yohane M’batizi anamutcha Yesu kuti “Mwana wa Nkhosa?”
-Mulungu anamupereka Yesu kuti adzaŵafere anthu onse ngati m’mene anaperekera mwana wa nkhosa kuti afe m’malo mwa Isaki.

-Pamene Yohane M’batizi anamaliza kumubatiza Yesu, Mulungu Mzimu Woyera anamutsogolera Iye kupita ku chipululu.

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 4:1

1-Pambuyo pache Mzimu anamutsogolera Yesu kupita ku chipululu kuti akayesedwe ndi Satana.

-Kodi chinachitika ndi chiyani pamene Yesu anali mchipululu?
-Satana anamuyesa Yesu.
-Satana sasintha.
-Satana ndi oyipa kuyambira pachiyambi.

-Tsopano Satana anamuyesa Yesu ngati m’mene anamuyesera Adamu ndi Eva.

-Kodi chifukwa chiyani Satana anamuyesa Yesu?
-Chifukwa chakuti Satana ankafuna kuti Yesu achimwe.

-Kodi chifukwa chiyani Satana ankafuna kuti Yesu achimwe?
-Chifukwa chakuti Satana sankafuna kuti Yesu aŵapulumutse anthu.

-Yesu anakachimwa, sibwenzi atatha kuŵapulumutsa anthu.
-Yesu anakachimwa, sibwenzi atatha kuŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana.

-Satana amkafuna kumugonjetsa Yesu amene anali Mulungu Mpulumutsi.
-Satana ankafuna kumupanga Yesu kukhala kapolo wache.

-Yesu anali mchipululu ndipo anakhala masiku 40, usana ndi usiku

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 4:2

2-Pa masiku 40, Yesu sanadye kanthu kalikose, usana ndi usiku, pambuyo pache inamukola njala.

-Ngakhale kuti Yesu anali Mulungu weniweni, Iye analinso Munthu weniweni.
-Ichi ndiye chifukwa chache Yesu inamukola njala.



Mulungu Atate kukamuyesa?
-Chifukwa chakuti Mulungu amanena zowona.
-Chifukwa chakuti Mulungu sanama.
-Chifukwa chakuti Mulungu amasunga malonjezo ache.
-Chifukwa chakuti Mulungu saphwanya malonjezo ache.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu sanalumphe kuchokera pamwamba pa Nyumba ya Mulungu?
-Chifukwa chakuti Mulungu Atate samuwuze Iye kuti achite zimenezo.

-Yesu sanamumvere Satana.
-Yesu anamumvera Mulungu Atate yekha.

-Kodi mayesero achitatu amene Satana anamuyesa Yesu anali otani?

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 4:8-9

8-Ndipo pomalizira Satana anamutenga Yesu ndi kupita naye pamwamba pa phiri lalitali kwambiri. Pamenepo anamuwonetsa ufumu onse wa pa dziko la pansi ndi ulemelero wache,
9-ndipo anamuwuza kuti, “Ndidzakupatsa zonsezi ngati ukundigwadira ndi,kundipembedza.”

-Satana anamutenga Yesu ndi kupita naye ku phiri lalitali kwambiri, ndipo anamuwonetsa Yesu ufumu onse wa pa dziko la pansi ndi ulemelero wache.

-Satana anamuwuza Yesu kuti amupatsa zonsezo

-Kodi Satana amachita chiyani ndi mawu a Mulungu?

-Satana amaŵasemphanitsa mawu a Mulungu kuti aŵatchere anthu.

-Kodi Satana anaŵasemphanitsa bwanji mawu a Mulungu kuti amutchere Eva?
-Satana anamuwuza Eva kuti safa ngati angadye chipatso chimene anaŵaletsa Mulungu.

-Satana anaŵasemphanitsanso mawu a Mulung kuti amutchere Yesu.

-Satana ankamuyesa Yesu kuti achite zina zache zimene Mulungu Atate sanamuwuze kuti azichite.
-Satana ankamuyesa Yesu kuti apange zinthu mosiyana ndi zochokera kwa Mulungu Atate, polumpha kuchokera pamwamba pa Nyumba ya Mulungu.

-Kodi Yesu anamuyankha kuti chiyani Satana?

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 4:7

7-Yesu anati, "Malemba akutinso kuti, "Usaŵayese Ambuye, Mulungu wako."

-Yesu anabwerezanso kwa Satana zimene zinalembedwa M'buku la Mulungu, Bayibulo.

-Yesu anamuwuza Satana kuti ife tisamutengere kokamuyesa Mulungu , Atate.

-Kodi chifukwa chiyani ife sitiyenera kumutengera



-Kodi mayeselo oyamba anali otani amene Satana anamuyesa Yesu?

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 4:3

3-Oyesa uja anafika ndikumuwuza kuti, "Ngati iwe uli Mwana wa Mulungudi, uyilamule miyalayi kuti isanduke kukhala mkate."

-Satana anamuwuza Yesu kuti, "Ngati iwe uli Mwana wa Mulungudi…"
-Kodi Satana sankadziŵa kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu?
-Inde.

-Kodi chifukwa chiyani Satana analankhula kuti, Ngati iwe uli Mwana wa Mulungudi…?"
-Chifukwa chakuti Satana ankamuyesa Yesu kuti atsimikiziredi kuti Iye anali Mwana wa Mulungudi.
-Chifukwa chakuti Satana ankamuyesa Yesu kuti achite chimene Mulungu Atate sanamuwuze kuti achichite.
-Chifukwa chakuti Satana ankamuyesa Yesu kuti achite zosiyana ndi zochokera kwa Mulungu Atate potembenuza miyala kukhala mkate.

-Kodi Yesu anakatha kutembenuza miyala kukhala mkate?
-Inde.

-Yesu anali Mulungu.
-Yesu anakatha kuchita china chilichose.

-Kodi Yesu anamuyankha chiyani Satana?

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 4:4

4-Yesu anati, "Malemba akuti, "Munthu sakhala ndi moyo chifukwa cha chakudya chokha, koma ndi mawu onse amene akulankhula Mulungu."

-Yesu anabwereza kwa Satana za zimene zalembedwa M'buku la Mulungu, Bayibulo.

-Yesu anamuwuza Satana kuti kukhulupilira Mawu a Mulungu ndi kofunika kwambiri kuposa zakudya.

-Kodi Yesu ankathandawuza kuti tisamadye?
-Iyayi.

-Yesu akudziŵa kuti ife tiyenera kudya zakudya kuti tikhale ndi moyo.

-Yesu anapanga zakudya kwa anthu onse.

-Yesu ankamuwuza Satana kuti moyo weniweni umachokera m'mawu a Mulungu.

-Ngakhale kuti Yesu anali ndi njala, kodi nanga chifukwa chiyani Yesu sanatembenuze miyala kuti ikhale mkate?
-Chifukwa chakuti Mulungu Atate sanamuwuze Iye kuti apange zimenezo.

-Yesu sanamumvere Satana.
-Yesu anamumvera Mulungu Atate.



-Kodi mayesero achiŵiri amene Satana anamuyesa Yesu anali otani?

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 4:5-6

5-Pambuyo pache Satana anamutenga Yesu ndikupita naye ku Yelusalemu, mzinda oyera. Ndipo anamuyimika pamwamba penipeni pa Nyumba ya Mulungu,
6-kenako anamuwuza kuti, "Ngati iwe uli Mwana wa Mulungu, udziponyele pansi. Pakuti malemba akuti, "Mulungu adzaŵalamulira angero ache kuti adzakuwakhe m'manja awo, kuti usadzaŵamenyetse mapazi ako pa miyala."

-Satana anamutenga Yesu ndikupita naye pamwamba penipeni pa Nyumba ya Mulungu ku Yelusalemu, ndipo anamuwuza kuti adziponyele pansi kuchokera pamwamba pa Nyumbayo.

-Satana anamuwuza Yesu kuti adziponyele pansi kuchokera pamwamba pa Nyumba ya Mulungu chifukwa chakuti kunalembedwa M'buku la Mulungu, Bayibulo, kuti Mulungu Atate adzamuthandiza Yesu.

-Kodi Satana ankazidziŵa zimene zinalembedwa M'buku la Mulungu , Bayibulo?
-Inde.

-Satana akuzidziŵa zimene zalembedwa M'buku la Mulungu, Bayibulo.